# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA, LA 2025-2026 M'BOMA LA NENO

## DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 ikuyembekezereka kukhala ya pakatikati, yosakhudzidwa ndi La Nina kapena El Nino.

Boma la Neno likuyembekezeka kulandira mvula ya **mlingo wokhazikika** mu nyengo ya dzinja ya 2025/2026.


## October 2025




M'mwezi wa October, boma la Neno likuyembekezereka kudzakhala lotentha ndi lopanda mvula m'madera ambiri. Koma madera ena atha kuzalandira mvula ya chizimalupsya yosaposera 30mm.

Mphenzi komanso mphepo yankuntho zikuyembekezerekanso


## November 2025




Mu mwezi wa November, madera ambiri m'bomali akuyembekezereka kuzalandira mvula yamlingo wapakati pa 50 ndi 100mm.

Mvulayi idzabwera yamabingu ndipo ndi mphepo yamkuntho.


## December 2025




Mvula yamlingo okwana 200mm ikuyembekezeleka kuzagwa m'madera ambiri ndipo pa Boma izagwa yochulukirapo pakati pa 250 ndi 300mm.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeleka kuzayamba sabata lachiwiri lamwezi wa December.


## January 2026




Mwezi wa January ukuyembekezekera kuzakhala ndi mvula yochulukirapo yamlingo wa 250-300mm m'madela ambiri.

Pali chiopsyezo cha ng'amba yasabata limozi.


## February 2026




Boma laNeno likuyembekezereka kuzalandira mvula yamlingo wapakati pa 150 ndi 200mm.


Pali kuthekera kwa ng'amba yosaposera sabata limodzi mu mwezi wa February.

## March 2026




Madela a mbiri mu boma la Neno akuyembekezereka kuzalandira mvula yokwanira 150 - 200mm.

## April 2026





Mu mwezi wa April madela ambiri akuyembekezera kuzalandira mvula yamlingo okwana 30 - 50mm.

Nyengo ya dzinja ikuyembezereka kupita kumapeto sabata lomaliza la mwezi wa April.

Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 ikuyembekezereka kukhala ya pakatikati, yosakhudzidwa ndi La Nina kapena El Nino.
Boma la Neno likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena mlingo woposera wokhazikika.
Nyengo yonse ya dzinja ikuyembekezereka kukhala masiku a pakati pa 120 kufika 130

Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu
.

| NENO | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 5.9 | 36.7 | 20.1 |
| NOV | 54.3 | 102.0 | 60.9 |
| DEC | 146.3 | 252.4 | 265.1 |
| JAN | 256.2 | 400.4 | 289.7 |
| FEB | 156.4 | 269.8 | 202.5 |
| MAR | 95.4 | 177.4 | 187.4 |
| APR | 25.0 | 61.6 | 37.3 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2025**

Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:
The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com